


MVERENI INU IYE

 Chachitika ndi chiyani? Ine ndikungodabwa. Kalekale, izo zinali zolakwika kuti mkazi avale chovala cha mwamuna. A...Ye...Baibulo linati, “Ndi chonyansa pamaso pa Mulungu.”

² Inu a Methodisti, ndikufuna ndithire moto pa inu: Pamene John Smith analalikira ulaliki wake womaliza, waufupi, maora foro, wokalamba kwambiri iwo amachita kumunyamula iye kupita naye pa nsanja, ndipo iye anati, “Oh, ine sindikudziwa chimene chiti chichitike, ngakhale ana aakazi a mpingo wa Methodisti akuvala mphete pa zala zawo.” Nanga bwanji tsopano atavala suti yosambira, atadzigoneka pa gombe pamaso pa gulu la amuna? Ndi inuyo a Methodisti.

³ Chabwino, inu a Baptisti: pemphero laling’ono apo ndi apo; ndipo John Smith, woyambitsa wa mpingo wa Baptisti, anapemphera mpaka maso ake anatupa ndikutsekeka, ndipo mkazi wake nkumachita kumutsogolera iye waku tebulo mmawa kuti akamudyetse kadzutsa wake. Manyazi pa inu a Baptisti!

⁴ Ndipo inu a Methodisti amene simumakhulupirira mu machiritso Auzimu: pamene John Smith (ine ndinaima pambali pa kachisi, osati kale kwambiri.), tsiku lina iye ankakwera kavalo wake, ndipo iye anadzagwa ndi kuthyola mwendo wake. Ndipo iye anatsika pa kavaloyo, ndipo anatenga botolo la mafuta kuchokera mthumba mwake ndipo anadzamudzoza kavalo ndipo nkudzamkweranso kumapita! Iwe kuti ulalikire zimenezo mu mpingo wa Methodisti ndipo iwo angakuponyere iwe panja pa chitseko. Oh, inu munathamanga bwino, nchiyani chinakutchingani inu?

⁵ Nditaima osati kale kwambiri, kwa mwamuna wamkulu wa Presbateria amene anaima pambali yanga, mu kagulu kenakake mu California. Iye anati, “Inu mukuganiza chiyani za zimenezo?” Iye sankandidziwa ine.

Ine ndinati, “Izo ziri bwino.”

⁶ Iye anati, “Inu mukudziwa, nthawi ina mpingo wa Presbateria unali mpingo wamphamvu ku Gombe la Kumadzulo.” Iye anati, “Koma kenako, kunadzabwera a Christian Science ndipo anadzangokhadzulira izo mzidutswa. Ndipo tsopano, apa pabwera bambo uyu, akuwakhadzulira a Christian Science mu zidutswa.”

⁷ Ndipo ine ndinanena, pamenepo, “Ngati inu mukanamawapatsa anawo Mkate wa Moyo, iwo sibwenzi atatsatira zinthu zoterozo ngati zimenezo. Koma ana anjala amakadya kuchokera ku dzala.” Dziko liri ndi njala lero

yofuna Mawu a Mulungu Wamoyo. Oh, anthu inu, chimene inu mukusowa, azibusa inu, ndi kudzidyetsa nkhosha zanu (Uko nkulondola.) Mawu a Mulungu Wamoyo.

⁸ Kenako Iye anapitirira kumanena mawu: “Oh, momwe ana Anu akumachitira izi.” Momwe Iye ayenera kuti amamvererera. Taganizani inu mutakhala mphunzitsi, ndipo nkupita kwa weniweniyo. . . Mpangi wanu, ndi kukanena za mwana Wake Yemwe, za momwe akukhalira.

⁹ Koma, tsopano, nanga bwanji ngati mwanayo atakhala kuti ndi mwana wabwino? Nanga bwanji ngati mwanayo amakhalira kuchita ntchito ya Atate? Ndiye Mphunzitsiyi angakhale wachisomo bwanji. Iye angabwere ndi kudzati, “Oh, wachikondi Bwana, mwana Wanu ali, basi, ‘chibanthu chochokera kwa chipika chakale.’ Iye ali chimodzimodzi basi monga Inu. Iye akumangokhala pa ntchito Yanu. Oh, Inu simudzampeza mwamuna wazamalonda wabwino wa Ufumu Wanu kuno kuposa mwana ameneyo.”

Momwe Atatewo angafufumire, “Oh, ameneyo ndi mnyamata Wanga. Oh, inde, iye ndi mwana Wanga wamwamuna.”

¹⁰ Momwe kuti Mzimu Woyera, utaima Pamaso pa Mulungu, umati, “Mwamuna uyu, iye ndi mwana weniweni. Iye akumakhala pa ntchito Yanu.” Iye timanena bwanji kuti tikukhala pa ntchito Yake? Ili ndiro dongosolo Lake: lalikira Mawu. “Ine ndikakwezedwa mmwamba, ndidzakokera anthu onse kwa Ine.” Momwe Iye angadzimvererere kupambana ndi kudzimva wokondwa.

¹¹ Kenako inu mukudziwa chimene chinachitika? Ngati mwana ameneyo sakukhala khalidwe labwino, iye sikuti amangokhala kuposa mwana wotayika kokha. Uko nkulondola. Tsopano, inu mukudziwa, ndine wa Chikalvinisti pang’ono pokha, koma ine—ine ndikukhulupirira ngati ndiwe mwana wobadwa wa Mulungu, iwe ukhoza kukhala mwana wosamvera, ndipo ungataye mphotho yako yonse, ndipo iwe sudzangokhala kuposa wa Baptisti wamba, Pentekoste, Nazarene kapena chirichonse chimene iwe uli. Koma, ngati iwe ungakhale tcheru ndi kumachita, ngati iwe ungamakhale womvera ndi kukhala mwana weniweni. . .

Tsopano Achilutera, pamene inu munadzapeza koyamba ‘olungama adzakhala moyo ndi chikhulupiriro,’ inu munapanga chiphunzitso kuchokera pamenepo. Uko nkulondola.

¹² Ndipo inu a Methodist, mwamsanga pamene a John Wesley anadzabwerapo, Lawi la Moto, pamene Ilo linkasuntha, iwo anadzamanga panso pa Ilo. Ndipo pamene a John Wesley anadzabwerapo, inu munadzapeza kubadwa kwatsopano, kapena chimene iwo amachittha kuyeretsedwa, ntchito yotsimikizika yachiwiri ya chisomo. Zimenezo zinali zabwino,

chomwechonso kulungamitsidwa kunali kwabwino. Koma, mwamsanga pamene inu munadzapeza kuyeretsedwa, inu munadzalemba mzere waung'ono, kapena, atsogoleri anu anatero, itachitika imfa ya Wesley, ndi Asbury, ndi ena otero, ndipo kenako inu munadzapanga chiphunzitso kuchokera pa zimenezo, ndipo inu munadzalemba mzere wa malire. Mulungu anangodzachotsapo Lawi la Moto.

¹³ A Pentekoste anadzazipeza zimenezo, kubwezeretsa kwa mphatso. Iwo anayamba kuyankhula mmalirime. Inu munapanga chiphunzitso kuchokera pamenepo, ndipo munadzalembapo chopumulira. Tsopano, Mzimu Woyera ukusunthira chitsogolo ukuchokapo, ndipo ukukusiyani inu. Uko nkulondola.

¹⁴ Oh, m'bale, pamene inu mudzilekanitsa nokha kuchoka kwa okhulupirira ena onse, Mulungu amadzachokapo. Inu mukuyenera kukondana wina ndi mzake. "Ichi anthu onse azadziwa kuti inu ndi akuphunzira Anga, pamene inu mukondana wina ndi mzake." Pamene a Methodisti ndi a Baptisti ndi a Lutheran ndi a Pentekoste angagwirane dzanja ndi dzanja ndi kumayenda kupita chitsogolo, inu mudzawona kutsanalira kumodzi kwakukulu kwa Mzimu wa Mulungu kumene inu munayamba mwakuwonapo.

¹⁵ Mderekezi samasamala bola ngati ife tikuwomberana wina ndi mzake. "Oh, zipitirirani, mudzingomenyana, mudzingophana nokhanokha." Koma tiyeni ife tizigwirizana mu gulu limodzi lalikulu. Ndiye mudzawone zimene zingamachitike. Mudzawone zimene zingamapitirire.

¹⁶ Tsopano, ngati mwana uyu atakhala mwana wabwino bwino, ndipo iye nkukhala womvera, ndipo nkukhala wolimbikira, ndipo iye—iye amakonda kumachita zinthu zimene abambo anamusiira iye kuti azichita, ndiye mphunzitsiyu amabwera ndipo amadzati, "Oh, iye ndi mwana wabwino." Zikatero tsiku lina lake, mwanayo akadzakhala wausinkhu (Zimene mpingo ukanayenera kukhala, kalekale.), mwana uyu amabweretsedwa poyera pagulu, ndipo amakhala atavekedwa mwinjiro, mwinjiro wokongola. Ndipo onse ozungulira kumeneko amaitanidwa.

¹⁷ Tsopano, mvetserani mwatcheru, potseka. Ndipo anthu onse amasonkhanako; kutsogolo kwa chipata, kawirikawiri, nkumene zimachitikira. Iye ankapita kutsogolo kwa chipata cha mzinda, ndipo kumeneko iye amakamukhazikako mwana wakeyo pa malo okwera, ndipo amakamuveka iye, mwinjiro.

¹⁸ Ndipo alaliki inu apa, ine ndikukamba za kukhazikitsidwa kwa mwana, inu mukudziwa, mu Baibulo. Tsopano, mu Agalatiya, kapena, Aefeso 1:5, "Pakuti Mulungu anaticonzeratu ife ku kukhazikitsidwa, kapena, kuikidwa pamalo ana, mwa Yesu Khristu." Tsopano, iye anali mwana kuyamba ndi kuyamba,

koma tsopano iye ndi womvera kwambiri. Kaya ndi wa chipembedzo chiti; zimenezo ziribe chochita ndi izo. Ndi kumvera ku Mawu, kumvera kwa Mulungu.

¹⁹ Ndiyeno iye amadzakhazikidwa pa mpando wokwera uwu, ndipo pamenepo pamadzakhala chisangalalo chachikulu ndipo abambo amamukhazikitsa mwana wake yemwe amene anali mu banja lake zaka zonsezi, amadzamukhazikitsa iye m'banja lake. Mwa kuyankhula kwina, iye amamukhazikitsa iye; amadzamupatsa iye malo ake m'banjalo. Ndiyeno zikachitika zimenezo, dzina la mwanayo limadzakhala chimodzimidzi basi pa cheke monga la abambo ake linali pakuti iye anali ataikidwa pamalo.

²⁰ Tsopano, abale anga a Pentekoste, Baptisti, Methodisti ndi Presbateria, chirichonse chimene inu muli, kodi inu mukuona pamene ife tikuperewera lero? Kodi inu mukuona? Ife timakangana kwambiri za chipembedzo chathu, zokhudza kutchuka kwathu, ndi za magulu athu; Mulungu sangachite nafe kalikonse. Ndife ana, koma, oh, mulole tsiku lifulumire pamene ife tidzakhoze kudzakhala pagulu la anthu ndi kudzavekedwa mu Mphamvu ya chirungamo Chake: kuti mawu athu, mapemphero athu adzachiritse odwala; ndipo kulalikira kwathu kudzapulumutse otayika; ndipo zizindikiro zazikulu ndi zozizwitsa za Baibulo zidzabwezeretsedwenso ku Mpingo kenanso. Pamene ife tidzaphwasulire pansu kusiyana kwathu kwakung'ono, kutsutsana kwachibwana, ndi pamene Mulungu ati adzachte izi.

Zindikirani, iye amayikidwa pamalo ndipo kenako iye amadzakhala mwana wokwanira kwathunthu. Zikatero dzina lake limadzakhala chimodzimidzi. Kenako . . .

²¹ Umo ndi mmene zimakhallira ndi Mpingo, ngati ife tingachokeko ku zotsemphana zathu zazing'ono ndi kubwera kwa Khristu ndi kuiwala za dziko lakunja, kapena, kuiwala za zipembedzo zathu, ndi zina zotero, ndi kukhala ana omvera, ndi kumakhala pa ntchito ya Atate yopulumutsa miyoyo, ndi kumachita zinthu za Mulungu, pakapita kanthawi Mulungu adzatiika ife kumbali imodzi ndipo Iye adzatidzodza ife ndi Mzimu Woyera, ndipo tikadzatero ife tidzaikidwa pamalo mu Ufumu Wake. Ena ali ndi mphatso za nzeru, ena ali ndi chidziwitso, ena ali ndi mphatso za malirime, ena amalalikira Uthenga, ena ndi aneneri, ndi mphatso zina.

²² Koma, tsopano, Mulungu akuyendetsa mphatso mu Mpingo. Ine ndikhozanso kunena izi, izi ziri pa mtima wanga. Mwaona, ine sindikufuna kuti ndikupwetekeni inu, m'bale. Ine sindikufuna kuti ndikupwetekeni inu, mlongo. Koma mpingo wa Pentekoste, ndipo inu anthu a Full Gospel ndi mphatso izi, inu simumadziwa mmene mungamazilumulire izo. Izo ndi

mphatso; izo ndi zabwino bwino, koma inu mumabalalika nazo izo. Ziyikeni izo pamalo ake.

²³ Penyani, mphatso yoyambirira ndi nzeru. Izo zingakuchitireni ubwino wanji kukhala ndi nzeru ngati inu simukudziwa...kukhala ndi nzeru yodziwira mmene mungalamulire chidziwitso chanu? Zingakuchitireni ubwino wanji kuti muziyankhula mmalirime, ngati inu mulibe nzeru yodziwira kuti ndi liti, ndi motani, ndi kuziyika izo molondola? Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Izo zimachita ubwino wanji kulalikira machiritso Auzimu pamene izo zimangobalalika? Inu simukudziwa chimene...

²⁴ Ine ndinati, “Ine ndakumanapo ndi magulu awiri a anthu mmoyo mwanga, ndipo amenewo ndi achikhazikitso ndi a Pentekoste.” Achikhazikitso mwa pamalo amadziwa chimene iwo ali, koma iwo alibe chikhulupiriro chirichonse. Mawu sanatengebe mizu mpaka pano, Iwo sanabwere nkomwe kudzakhala Moyo. Koma mwa pamalo, iwo amadziwa pamene iwo ali. Achipentekoste ali ndi chikhulupiriro, koma iwo samadziwa chimene iwo ali. Izo ziri ngati, munthu amene ali ndi ndalama ku banki, osamadziwa mmene angalembere cheke, ndipo enawo akhoza kulemba cheke, ndipo alibe ndalama mu banki. Ngati inu mungathe kuwabweretsa amenewo pamodzi.

O, Mulungu, tipatseni ife mwina mpingo wauzimu wachikhazikitso, kapena mpingo wachikhazikitso wa Pentekoste.

²⁵ Inu muli ndi chikhulupiriro chochuluka, koma inu simumadziwa basi mmene mungachiyikire icho; icho chimangobalalika. Mwanjira imeneyo izo zimabweretsa chitonzo mochuluka kuposa mmene izo zimachitira bwino. Muziike izo mu Baibulo. Ichi ndicho Choyang’anapo; osati zimene anthu akufuna, koma zimene Mulungu akufuna. Mugwirizane ndi dongosolo Lake. Ndiko kusiyana kwake; ndi chifukwa chake ife sitikupita mmene ife tikuyenera kuchitira, abwenzi.

²⁶ Tsopano, pamene anali ataima pamenepo, zindikirani, kuti atakhala Pamaso pa Mulungu...Tsopano, mu Chipangano Chakale, Mulungu sankamufunsa munthu kuti achite chirichonse pokhapokha Iye atachita icho Iyemwini. Pamene munthu agamulidwa kuti apshedwe, kuti akafe, njira yokhayo imene Mulungu akanamuwombolera iye ndi kudzatsika mthupi, ndi kudzatenga malo ake.

²⁷ Ndi chifukwa chimene ine ndinalalikira mmene ndinachitira usiku wapitawu: Khristu ndi woposa munthu; Iye ndi Mulungu; Iye an kayenera kutsika pansu, ndi kudzavala thupi kuti adzalawe tchimo; Iye sakanamutumiza munthu wina; Iye sakanakhala wolungama pochita chomwecho; Iye an kayenera kuti abwere Iyemwini. Ndipo Iye anadzamuphimba namwali,

ndipo analenga khungu la Magazi limene linadzabala Mwana, ndipo Mulungu anadzakhala mwa Mwanayo, anadzakhala mkachisi kuno pa Dziko lapansi. Iye anali *Emmanuele*, osati mneneri, koma “Mulungu nafe!” Mulungu anali mwa Khristu akuyanjanitsa dziko kwa Iyemwini. Inali njira yokhayo imene Iye akanadzalawa tchimo ndi imfa, inali kuti adzapangidwe kukhala wachivundi monga munthu.

²⁸ Muwomboli wachibale wa Rute, amene ine ndamulalikirapo mochuluka kudutsa fukoli, monga inu mwinamwake munawerengera maulaliki; oh, iye ankayenera kukhala wachibale kuti akhale muwomboli. Ndipo njira yokhayo imene Mulungu akanakhala Muwomboli, Iye ankayenera kudzakhala Wachibale kwa ife. Ndipo Iye anadzakhala mnofu ndipo anadzakhala pakati pathu. Iye ndi Wachibale wathu. Iye anali Munthu wa mnofu monga ine ndiliri, monga inu, koma, Mulungu anadzakhala mwa Iye kuti adzazunzike ndi kudzamverera, kudzalawa, akugwiritsa ntchito zokhudzira zisanu monga momwe ife tiriri. Iye anadzakhala Muwomboli.

²⁹ Ndipo kenako, pamene Iye anaima pamenepo pa Phiri la Chiwalitsiro, Mulungu anali kuwonetsera kwa dziko chimene Iye anamufunsa munthu kumbuyo kuti adzachite kumbuyo uko pansu pa kukhazikitsidwa kapena kuikidwa pamalo kwa ana.

³⁰ Petro anasangalala kwambiri. Kawirikawiri anthu amatero pamene iwo akhala mu Kukhalapo kwa Chauzimu. Kawirikawiri iwo amalephera kuti adzigwire okha chifukwa iwo ndi zolengedwa za pa dziko lapansi, ndipo komabe, iwo ndi zolengedwa za Kumwamba, nawonso. Koma kulawiratu kumeneko kumangowasokoneza iwo.

³¹ Ndicho chimene chinachitika kwa mpingo wa Pentekoste. Mukuona? Kulawiratu kumeneko, iwe sumadziwa mmene ungadzigwirire wekha. Kulingalira konse kumakutherani. Inu simumadziwa mmene mungaziyikire mphatso za malirime zimenezo pa malo, kutanthauzira kumeneko. Pamene mlaliki akuyankhula, nthawizina, iwo amadzuka pomwepo ndi kumayankhula, pomwepo pamene mlaliki akuyankhula. Zimenezo ndi zotsutsana ndi Baibulo. Ndipo inu mumati, “Oh, Mulungu anapereka uthenga wa *ichi*. Izo ndi zatsopano kuposa Baibulo.” Ayi, izo si choncho! Kutu . . .

³² Mawu anu adzalephera, ndipo china chirichonse chidzalephera, koma Baibulo linati, “Ngati pali wauzimu aliyanse kapena mneneri pakati panu, muloleni iye avomereze kuti chimene ine ndikulemba ndi malamulo a Mulungu.” Ndipo, “Ngati Mngelo wochokera Kumwamba angalalikire uthenga wina uliwonse wosiyana ndi umene walalikidwa, muloleni iye akhale wotembereredwa.” Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza?

³³ Chotero, ngati inu mumayesetsa kuti mugwirane chanza ndi anthu kuti muwabweretse iwo mu Ufumu wa Mulungu, inu mukulakwitsa. Iwo amachita kubadwira kulowa mu Ufumu wa Mulungu mwa Mzimu Woyera. Iwo samabatizidwa nkhope itayang'ana kutsogolo, kumbuyo, kukonkhedwa, kutsanuliridwa, mu dzina limodzi kapena limzake. Iwo amabadwa mwa Mzimu wa Mulungu kukalowa mu Ufumu wa Mulungu.

³⁴ Petro anasangalala. Iye anati, “Ambuye, tiyeni timange misasa itatu. Ife timange umodzi wa Mose ndi onse ofuna azisunga lamulo. Mose ankaimira lamulo. Onse amene akufuna kuti azisunga lamulo, malamulo, ndi osadya nyama, ndi zina zotero, asiyeni iwo azichita zimenezo. Ndipo ife timanga umodzi wa Eliya. Ndipo timanga umodzi wa Inu.”

³⁵ Tsopano, Mose ankaimira lamulo, malamulo onse. Ndipo palibe munthu amene angapulumsidwe ndi lamulo. Lamulo silinali mpulumutsi, lamulo linali mphunzitsi wa sukulu. Lamulo linali chilango. Lamulo linkakulitsa tchimo. Mwakuyankhula kwina, lamulo linali nyumba ya ndende, kuti Mzimu unkakuikani inu mu nyumba ya ndende, koma, ilo silinkawombola; ilo linalibe kanthu mkati mwake koti kawombolere. Yesu anali Muwomboli. Tsopano, Mose ankaimira lamulo. Mwa lamulo, palibe mnofu uti udzapulumutsidwe. Ndi chifukwa chake Iye anabweretsa mboni zitatu kuchokera Kumwamba.

³⁶ Tsopano, Eliya ankaimira chirungamo cha Mulungu. Ndipo m'bale wanga, kodi iwe ungayerekeze kunena kuti ukufuna chirungamo kuchokera kwa Mulungu? Pamene iwe unabadwa mu tchimo, unawumbidwa mu kusaeruzika, unabwera mu dziko ukuyankhula mabodza. Ndipo iwe ukufuna chirungamo? Mulungu anati, “Tsiku limene inu mudzadya icho, tsiku limenelo inu mudzafa.” Izo zikukhazikitsa izo. Inu mwapeza chirungamo, inu mwathedwa.

³⁷ Ndipo lamulo? Lamulo limangozibweretsa izo pamaso panu, limati, “Apa, iwe wamangidwa; iwe unachimwa; iwe unapanga mphulupulu; ndipo ndende yako yatsegulidwira iwe, gehena yeniyeniyo: pita ukalowe mmenemo.” Ichu ndi chimene lamulo linkanena.

Ndipo chirungamo sichinkafuna nkomwe lamulo. Mawu amakhala kuti ayankhulidwa kale. Ndizo zonse. Mulungu ayenera kumasunga Mawu Ake.

³⁸ Tamuwonani Eliya, wa Mulungu... iye anali mpita wa Mulungu wa chirungamo. Iye anali atakhala pa phiri, iye anati, “Ngati ine ndiri munthu wa Mulungu,” pamene mtsogoleri wa fifite ameneyo abwera, anati, “Moto ubwere kuchokera Kumwamba.” [M'bale Branham akukhwatchitsa zala zake—Mkonzi]. Pamene, pameneyo fifitewo anapita.

39 “Chabwino,” mfumu inati, “mwina mphezi inawakantha iwo. Oh, ine sindikhulupirira mmasiku a zozizwitsa, chotero mwinamwake inali mphezi kapena chinachake chinawakantha iwo; izo zinangochitika mwangozi basi. Ine nditumiza fifite ena.”

40 Mneneri wolimba ameneyo, wokalamba wa chirungamo anaima pamenepo, ndipo anati, “Ngati ine ndiri munthu wa Mulungu, mulole Moto ubwere kuchokera Kumwamba.” Ndipo pansi moto unadzatsika, ndipo unadzanyeketsa fifite ena. Siinali ngozi, pamenepo. Bwanji? Iye anali mpita wa chirungamo cha Mulungu.

Ayesere aliyense wa inu kuimikana ndi chirungamo cha Mulungu. Ayesere aliyense wa inu kupita Kumwamba mwa lamulo. Taonani pamene ife taima.

41 Petro anati, “Tiyeni timange misasa itatu.” Tayang’anani pa mdima. Ife tathedwa kuchokera pa chiyambi. Chirungamo cha Mulungu chimafuna chobwezera; chobwezera chimafuna mphotho; mphothoyo ndi imfa. Lamulo limakuza izo ndipo limatiponyera ife kuti tikamangidwe ndi kutiika ife mndende. Ndi chithunzi cha mdima bwanji kwa mtundu wa anthu.

42 Koma, oh, mzanga wokonededwa, wosauka, wolema, tembenuzira mutu wako mbali iyi. Pamenepo panadzaima Yesu. Yesu wokulitsidwa, monga ankakhalira mwana kumbuyo uko pansi pa Chipangano Chakale. Iye anapatsidwa ulemelero, mongoyembekezera. Oh, zovala Zake zinawala ngati dzuwa, ndipo Liwu kuchokera Kumwamba linati, “Uyu ndi Mwana Wanga wokonededwa; mvereni inu Iye.”

43 Chotero, zipembedzo zathu zonse, zokhumudwitsa zathu zonse, kutsemphana kwathu konse sikutanthauza kanthu. Yesu anaimirira chikondi cha Mulungu. “Mulungu analikonda kwambiri dziko lapansi, Iye anampereka Mwana Wake wobalidwa yekhayo, kuti aliyense amene akhulupirira mwa Iye asadzafe, koma adzakhale nawo Moyo Wamuyaya.”

44 Chotero izo sizimakhala mu chirungamo. Izo sizimakhala mu lamulo kapena chimene iwe wachita. Izo zimakhala mu chifundo ndi chikondi cha Mulungu, kuti Khristu anabwera pa dziko lapansi ndipo anadzatenga malo anu.

45 Mulungu Mwiniwake anati, “Tsopano taonani, ine ndilengeza izi pamaso pa Kumwamba: Palibe munthu amene angapulumsidwe ndi lamulo, izo zachitika. Ine ndizilengeza izo pa dziko lapansi palibe munthu amene angapulumsidwe ndi lamulo, palibe munthu amene angapulumsidwe ndi chirungamo. Koma, ‘Uyu ndi Mwana Wanga wokonededwa.’ Palibe munthu angapulumsidwe pokhala wa mpingo wa Baptisti. Palibe munthu amene angapulumsidwe pokhala wa mpingo wa Methodisti. Palibe munthu amene angapulumsidwe pokhala wa mpingo wa Pentekoste. Koma,

‘Uyu ndi Mwana Wanga wokondedwa, mwa Iye Ine ndikondwera kukhalamo. Mvereni inu Iye.’”

⁴⁶ Chifukwa chiyani mvereni inu Iye? Iye ndi Mmodzi yekhayo amene angapulumutse. Iye ndi Mmodzi yekhayo amene angapereke mtendere. Iye ndi Mmodzi yekhayo amene angachiritse. Lamulo silingachiritse; ngakhalenso chirungamo sichingafune. Koma Mwana wa Mulungu akhoza kupulumutsa ndi kuchiritsa ndi kupereka mtendere. Pakuti, “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, anatunduzidwa chifukwa cha mphulupulu zathu: chilango cha mtendere wathu chinali pa Iye; ndipo ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Mvereni inu Iye.

⁴⁷ Ngati ndinu wa Methodisti, mukhale pomwepo, koma mvereni inu Iye. Ngati ndinu wa Pentekoste, khalani pomwepo, koma mvereni inu Iye. Chirichonse chimene icho chiri, kulikonse kumene inu muli wa kumeneko, izo ziribe kanthu kochita ndi zimenezo. Ngati ndinu mwana wobadwa mwatsopano wa Mulungu, ndipo wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo ndinu wa Roma Katolika, mvereni inu Iye. Mulungu adzasamalira zina zonse za izo. Inu muzingomumvera Iye, ndipo Mulungu adzasamalira zina zonsezo.

⁴⁸ Chimene ife tikuchisowa lero, abale, mu ndemanga yanga yotsiriza potseka ndi iyi: Ife tikusowa wotibhetchera. Ife tikusowa winawake woti atiwonetsere chikondi cha Mulungu. Ife tikusowa mpingo winawake, magulu ena a anthu. Chigwa ichi, kuno, chikusowa gulu la anthu, gawo lirilonse la dziko likusowa gulu la anthu kuti adzawonetsere kudzipereka kwenikweni uko kumene Mulungu wakuphimbani nako inu mwa Mzimu Woyera, ndipo anakupatsani inu chikondi. Kumene . . .



MVERENI INU IYE CHA57-0317

(Hear Ye Him)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu madzulo, Marichi 17, 1957, ku Lake County Fairgrounds mu Lakeport, California, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2021 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org